Baibulo ya ana
Ikupasilani



Kumwamba,
kunyumba
yokongola
ya Mulungu

Yolembedwa ndi: Edward Hughes

Yojambulidwa ndi: Lazarus

Yotengedwa ndi: Sarah S.

Yotathauzidwa ndi: Phiri Williams

Yo pangidwa ndi: Bible for Children
www.M1914.org

©2013 Bible for Children, Inc.
Chilolezo: Muli ndi ufulu wotenga ndi kuchurukitsa makopewa koma osagulitsa.

Pamene Yesu anakhala padziko la psansi anaphunzitsa ophunzira ake za kumwamba. Anatchulako kuti "Nyumba ya Atate wanga",

ndikunena kuti muli malo ambiri.

Nyumbayi ndimalo, okongola.
Kumwamba ndinyumba
yayikulu yokongola
kuposa manyumba
onse apadziko
lapansi pano.

Yesu anati, “Ndipita kukakukhonzerani malo.

Ndipo ngati ndikupita kukakukonzerani malo inu, ndizabweranso kuzakulandirani inu kwa ine.”

Yesu anapita kumwamba, atawuka kwa akufa.

Pamene ophunzira amamuwona, Yesu anatengedwa, ndi mtambo unamulandira iye kuchoka mmaso mwawo.

Kuchokera nthawi imeneyo,
Akirisitu akumbukila lonjezo
yakubweranso kwa
Yesu kuzawatenga.

Yesu anati ndidza bwela modzidzimutsa, pamene simukuyembekedzera.



Koma zikhala bwanji Akhristu akufa iye asanabwere? Baibulo ikuti amapita kukhala ndi Yesu. Kusapezeka mthupi ndi kupezeka ndi Ambuye.

Chibvumburutso, buku lomaliza mbaibulo, limatiwuza ife mmene kumwamba kulili.



Chinthu chokondweretsa ndiyichi, njira yapadera, kumwamba ndi nyumba ya Mulungu. Mulungu alipena paliponse, koma mpando waufumu wake uli kumwamba.



Angelo ndi zolembedwa zina zammwamba alambira Mulungu kumwamba.

Ndi anthu onse a Mulungu anafa ndikupita kumwamba. Amayimba nyimbo zapadera zotamanda Mulungu.



Mau mwa ena womwe amaimba ndi awa: MWAYENERA CHIFUKWA MWATIWOMBOLA NDI ...



… MWAZI WANU KUCHOKERA KUMAFUKO ONSE NDI MITUNDU YONSE …

... NDIKUTIPANGA IFE MAFUMU NDI ANSEMBE A MULUNGU.
(Chibvumbulutso 5:9)

Kumapeto a baibulo kumatimasurira kuti kumwamba ndi “Yerusalemu wa tsopano”. Ndikwa kukulu, kukulu kwambiri,



ndilinga lalitali.

Linga ndiya myala ya Yaspi, yoonekera ngati madzi. Zobvala zamtengo wapatali wonyezimira ndimawonekedwe



wosiyana siyana.

Mzinda wuli wonse unapangidwa umodzi koma waukulu ndimaonekedwe abwino!



Ndimakhomo ake apamwamba samatsekedwa. Tiyeni tonse tilowe ndikuzungulira mkatimo...
WAA!

Kumwamba ndikokongola koposa mkati. Mzinda wopangidwa ndi Golide woyenga, galasi. Ngakhale njira zake ndiza Golide.



Kukongola, msinje
wamadzi wa moyo uyenda kuchokela
kumpando wachifumu wa Mulungu.
Kumbali zonse zonse ya msinjewu kuli
mtengo, womwe unapezeka mumunda
wa Edeni.



Mtengo umenewu ndiwofunikira kwambiri. Umabereka zipatso khumi ndi ziwiri zosiyana siyana pa chaka. Ndipo masamba amtengo wa moyo ndi wochiritsa maiko.



Kumwamba sikufunikanso kuwala kwa zuwa kapena mwezi. Ulemelo wake wa Mulungu umawala koposa. Kulibe usiku kumeneko.



Ngakhale nyama kumwamba ndizosiyana. Ndizozolowerana. Zimbalangondo zimadyela limodzi ndi nkhosa.



Ngakhale mkango umadya limodzi ndi n'gombe. Ambuye akuti, "sipazakhala kuwawa kapena kuwononga paphiri langa loyera."



Tikuwona bwino bwino, tadziwa kuti pali zinthu zosowekela kuchokera kumwamba.

Kulibe mau awukali ungamve. Kulibe kumenyana kapena kuzikonda.

Kulibe maloko pa dzitseko, chifukwa kulibe mbava kumwamba.

Kulibe abodza, akupha, amfiti, ndi anthu ena woyipa. Kulibe chimo ina iliyonse kumwamba.

Kumwamba kuli Mulungu kulibe misozi. Thawi zina, anthu a Mulungu amalira chifukwa cha zowawa za moyo. Ku Mwamba, Mulungu azapukuta misozi yonse.

Kulibe imfa kumwamba. Anthu a Mulungu azakhala ndi Ambuye kwa nthawi zonse.

Kulibenso kulira, kulibenso maliro, kulibenso ululu.



Kulibenso kudwala, kulibenso kusiyana. Wina aliyense ndiwokondwa ku Mwamba ndi Mulungu.



Zopambana kwa zonse,
Kumwamba anyamata ndi
atsikana (ndi akulunso)
amene akhulupirira Yesu
Khristu ngati
mpulumutsi
ndi kumvera
iye ngati
Mbuye.



Kumwamba kuli buku yochedwa Buku ya moyo la Nkhosa. Ndilozaza ndi maina ya anthu. Kodi mukuziwa maina analembedwa mmenemo?



Anthu wonse anayika chikhulupiliro chawo mwa Yesu. Kodi dzina lako lalembedwa mmenemo?



Mau omalizila mu Baibulo onena za kumwamba akutiyitana ife. “Ndipo Mzimu ndi mkwatibwi akuti, ‘Bwera!’



ndipo amene amva anene 'Bwera!' Ndipo iye wakumva ludzu abwere. Ndiwomwe akukhumba, atenge madzi a moyo mwaulele."



Kumwamba, kunyumba yokongola ya Mulungu

Nthano yochokera mu mau a Mulungu, Baibulo,

opezeka mu

Yohane 14; 2 Akorinto 5;
Chibvumbulutso 4, 21, 22

“Polowela pa mau anu pamapasa kuwala.”
Masalimo 119:130

Mapeto

Nthano iyi yamBaibulo imakamba za ubwino wa Mulungu yemwe anatipanga ndipo akufuna kuti mumdziwe iye.

Mulungu amadziwa kuti tima chita zoipa, zimene zimachedwa chimo. Chilango cha uchimo ndi infa, koma Mulungu anatikonda kwambiri ndipo anatuma mwana wake yekha, Yesu, kuzatifela pamtanda ndi kunzunzika chifukwa cha machimo anu. Ndipo anaukanso kwa akufa na pita kumwamba! Ngati ukukhulupirira Yesu mupempheni akukhululukileni machimo anu, azakukhululukirani! Adzabwera kukhala nanu, ndipo muzakhala naye kunthawi zonse.

Ngati mukukhulupirira kuti izi ndizoona, nenani ichi kwa Mulungu: Ambuye Yesu, ndikhulupirira ndinu mwana wa Mulungu, ndipo munakhala munthu kundifera ine machimo yanga, ndipo mulinso ndi moyo. Chonde, lowani mmoyo mwanga ndikundi khululukira machimo anga, kuti ndikhale ndi moyo watsopano, ndipo tsiku lina ndikakhale ndiinu muyaya. Ndithandizeni kukumverani ndi kukhala mwa inu ngati mwana wanu. Ameni.

Welenga Baibulo ndi kuyankula ndi Mulungu matsiku onse! Johane 3:16